**Ministry of Finance, Economic Planning and Decentralisation**

# *Chidziwitso*

## KAPEREKEDWE KA NDALAMA ZA MU THUMBA LA CHITUKUKO CHA M'MADERA (CONSTITUENCY DEVELOPMENT FUND – CDF)

Unduna wa za Chuma ukudziwitsa a Malawi onse kuti ndondomeko yopereka ndalama za thumba la chitukuko ku madera onse a Aphungu (Constituency Development Fund – CDF) ikadali mchimake ndipo ndondomekoyi idayamba kumayambiriro a chaka cha chuma cha Boma cha 2026/27 ndi ndalama zothandizira kuti maKhonsolo (Local Councils) akwanitse kukonza ndondomeko za chitukuko m'madera awo. A Malawi akudziwitsidwanso kuti ndondomeko zoperekera ndalama za chitukukozi zinasinthidwa. Mwachitsanzo, pomwe mu thumba la chitukuko la kale la CDF ndalamazi zinkaperekedwa ku maKhonsolo ndondomeko zachitukuko zisanadziwike, mu ndondomeko yatsopano, maKhonsolo akuyenera kumaliza kukonza ndondomeko za momwe ndalama zikagwirire ntchito ndalama zachitukukozo zisanaperekedwe. Mundondomeko yakaleyi, ma Khonsolo ankaloledwa kukonza ndondomeko ya chitukuko chawo atalandira kale ndalama; koma mundondomeko yapanoyi, sakuloledwa kutero pokhapokha amalize kukonza ndondomeko za momwe ndalama zomwe alandire zikagwirire ntchito. Ndondomeko zonse zachitukuko zikamalizika ndikupeza omwe akagwire ntchito, ndalama zidziperekedwa zothandizila kuti omwe asankhidwa kugwira ntchito (ma contractor) ayambe ntchito. Izi zikatheka, ndalama zotsalira zidziperekedwa potsatira kafukufuku wokwanira wofotokozera momwe ndalama zoyamba zija zagwirira ntchito. Boma likudziwitsa onse okhudzidwa kuti ndondomeko imeneyi ikuyenera kutsatidwa ndipo madulira a mtundu wina uliwonse sadzaloredwa pofuna kuteteza chuma cha Boma kwa akamberembere omwe amafuna kulowererapo nkusokoneza chitukuko cham'madera.

Tafuna kudziwitsanso a Malawi kuti pofika pa 1 July 2026, simakhonsolo onse omwe anali atamaliza kupanga ndondomeko za zitukuko zomwe akonza kuti achite mundondomeko ya thumba la chitukuko ya CDF. Komabe, ena mwa maKhonsolowa anali atakwanitsa kulongosola zitukuko zomwe apange ndipo adayamba ndondomeko yopeza omwe adzawagwirire ntchitozo. Tati titsimikizire mtundu wa a Malawi kuti maKhonsolowa akapeza omwe adzawagwilire ntchito, ndalama zoyambirira ziperekedwa kuti zitukuko zomwe ayala ziyambe. Choncho, nkusokoneza anthu kumanena kuti kupereka ndalama za thumba la chitukuko cha CDF yachedwa pomwe zoyenera kutsatidwa kuti ndalamazi ziperekedwe sizinamalizike.

A Malawi onse akudziwitsidwanso kuti Unduna wa za Chuma wakhala ukupereka ndalama zothandizira kukonza ndondomeko za chitukuko cha m'maderazi kuyambira mwezi wa May 2026 ndipo pofika kumapeto a mwezi wa June 2026 tinali titapereka ndalama zokwana **MK7,866,318,182** ku maKhonsolo osiyanasiyana. Zindikirani kuti ndalama zomwe takhala tikuperekazi ndi gawo limodzi la ndalama zomwe zikuyenera kupita ku madera onse a dziko lino mu ndondomeko ya chitukuko chakumaderayi (CDF). Unduna wa za Chuma upitiriza kupereka ndalama zoyendetsera chitukuko kumaKhonsolo onse motsatira dongosolo lomwe ma Khonsolowa adatipatsa. A Malawi akudziwitsidwanso kuti ndalama za ngongole zomwe zipindulire achinyamata komanso azimayi, zidayamba kale kuperekedwa ku bungwe lobwereketsa ndalama la Malawi Enterprise Development Fund (MEDF).

Mwa ichi, Boma la Malawi likutsimikizira mtundu wa Malawi kuti kupereka ndalama zachitukuko cha thumba la chitukuko cha ku madera (CDF) kukuyenda monga mwa chikonzero chake ndipo Unduna wa za Chuma ndiwodzipereka kuwonetsetsa kuti ndalama za thumba la chitukuko la CDF zikuperekedwa mu nthawi yake kuti ndondomeko za chitukuko zomwe maKhosolo akoza ziyende bwino.

**Peterson Ponderani**
Principal Secretary for Decentralisation
Ministry of Finance, Economic Planning and Decentralisation